# BOMA LATHU

*Kubweretsa Nkhani Mkhonde Lanu*

VOL. 47 NO. 1 | *YAULERE* | Boma Lathu, Epulo, 2024


# Tilemekeze Malamulo

## Ndikofunika kulimbikitsa chitetezo - Chakwera


WOLEMBA: MEMORY CHATONDA


CHITETEZO ndi chofunika kwambiri kuti dziko litukuke mmagawo osiyanasiyana. Dziko lomwe anthu ake salemekeza malamulo silingapite mtsogolo pachitukuko.

Posachedwapa tsogoleri wa dziko lino a Dr Lazarus Chakwera anatsimikizira Amalawi kuti boma layika chidwi powonetsetsa kuti malamulo akutsatidwa mdziko muno.

Mtsogoleriyu analankhula izi ku kusukulu ya apolisi ku Limbe pamene apolisi okwana 1,367 amamaliza maphunziro awo amiyezi khumi, pomwe anati apolisiwo tsopano ndiokonzeka kukagwira ntchito yoteteza Amalawi ndi katundu wawo mmadera osiyanasiyana mdziko

TSAMBA 2

ZA CHITETEZO



Wojambula: Arkangel Tembo

*Pulezidenti Chakwera kuyendera pelete*

ZA ULIMI

## Ulimi wa Chamba udzichitika motsata malamulo


WOLEMBA: TWIMEPOKI MANGANI


DZIKO LA MALAWI ndi limodzi mwa maiko ochepa amene akhazikitsa malamulo a ulimi wa chamba muno mu Afirika. Powona kufunika kwa mbewuyi ku misika ya mayiko akunja, dziko la Malawi kwa zaka zingapo, lakhala likuwunika ndondomeko komanso malamulo amene angathe kuyendetsa bwino ulimi wa mbewuyi.

Posachedwapa, Nyumba ya Malamulo yavomera ulimi wa chamba chakwathu kuno ndi cholinga chakuti Amalawi azitha kuchita ulimi wa mbewuyi, yomwe yakhala yoletsedwa kwa nthawi yaitali ndikupeza phindu potengera mmene mbewuyi ikufunikira ku misika yakunja.

Nkhaniyi idawunikidwa kwambiri pazokambirana za pankumano wa Aphungu masiku apitawa ku Nyumba ya Malamulo, poganizira zovuta zimene zingabwere potsatira kuvomerezedwa kwa ulimiwu.

Phungu wadera lakumwera kwa boma la Lilongwe, a Peter Dimba, omwe adatulutsa ganizoli, adati ndi okondwa pakuvomera kwa aphungu palamuloli kumene kukusonyeza kufunika kwake kwa ulimiwu pachitukuko chachuma cha dziko lino.

"Tikufuna kupereka chiloledzo palamulo la ulimi wa chamba poyika ndondomeko zokhwima pakayendetsedwe ka ulimiwu. Mchaka cha 2018, tidayambitsa ulimiwu, koma mwanjira ina, tidausiya

TSAMBA 3



Mitengo yambewu yatsopano yapereka chimwemwe

TSAMBA 4



Ntchito yoteteza mtsinje wa Bua ili mkati

TSAMBA 10



Kanema ya chimalawi yatsopano ituluka posachedewa

TSAMBA 14

## Ndemanga

### Tithandize kupititsa patsogolo chitetezo

POSACHEDWAPA mtsogoleri wadziko lino Dr Lazarus Chakwera anali nawo pamwambo omwe apolisi atsopano amamaliza maphunziro awo ku sukulu ya apolisi ku Limbe. Mwambowu ndichitsimikizo choti boma liri ndi chidwi poonetsetsa kuti anthu komanso katundu mdziko lino ndi otetezedwa.

Posachedwapa kudzera mzionetsero zomwe ena akhala akuchita, Amalawi awona mmene kusatsata malamulo kumaonongera dziko pamene anthu amataya miyoyo komanso katundu kuonongeka.

Ichi ndichitsimikizo kuti kutsata malamulo ndikofunika pa chitukuko cha dziko. Kulemba ntchito kumene Boma lachita, kulimbikitsa chitetezo mdziko lino ndipo kuti anthu azikhala mwabata ndikumagwira ntchito zotukula miyoyo yawo mwantendere.

Chidwi chomwe Boma laonetsa potukula ntchito zachitetezo mdziko lino ndikofunika kwambiri pa miyoyo ya Amalawi. Koma chidwi cha boma pachokha sichikukwanira ngati Amalawi sangatengepo mbali poonetsetsa kuti mmadera momwe akuchokera muli bata ndi mtendere.

Apolisi paokha sangakwanitse kufikira paliponse kupereka chitetezo, iwo amadalira anthu mmadera powadziwitsa za anthu omwe amaphwanya malamulo mmaderamo.

Ife a Boma Lathu. Tikuyamika kwambiri mtsogoleri wadziko lino chifukwa choonesta chidwi pankhani zachitetezo mdziko lino, zomwe zikupangitsa kuti ntchito zambiri zachitukuko ziziyenda bwino. Chitetezo chokhwima chadziko lino chithandizira kwambiri kutukuka kwadziko mmagawo osiyansiyana ndikupereka mwayi kwa Amalawi ogwira ntchito zawo mwabata.

# Nthenda yamaso ikupitirira kufala

ZA UMOYO



Wojambula: Beatrice Bangula

Jobe - Pakufunika kudziwitsa anthu za nthendayi mokwanira

WOLEMBA:
BEATRICE BANGULA

PAMENE mliri wa ng'ombo (nthenda yakufiila kwa maso) ikufala mdziko muno, chiwerengero cha anthu omwe apekeza ndi nthendayi tsopano chadutsa 12,000.

Unduna wa zaUmoyo wati nthendayi yafika mmadera ambiri mdziko muno ndipo ena odwala nthendayi akhoza kukhala akhungu ngati sangalandire thandizo mofulumira.

Mneneri mu Unduna wa za Umoyo a Adrian Chikumbe ati pano matendawa afika pafupifupi m'maboma onse a dziko lino ndipo anati boma la Karonga ndi lomwe likutsogola pachiwerengero cha anthu omwe akupezeka ndi nthendayi motsatana ndi mzinda wa Lilongwe.

Chikumbe adaonjezera kuti Unduna waza Umoyo ukuyetsetsa kuthana ndi matendawa omwe zizindikiro zake ndi kufiira kwa maso, kuyabwa, kutuluka misonzi ndi kuwawa m'maso mwa zina.

"Matendawa amatha pawokha ndipo nthawi zambiri safunikira mankhwala mkati mwa masiku asanu ndi awiri mpaka khumi. Unduna wathu ukulimbikitsa anthu kuti azipita kuchipatala mwachangu akaona zizindikirozi ," adaonjezera a Chikumbe.

Iwo adaonjezeranso kuti Unduna wa za Umoyo ukuchititsa misonkhano komanso kukambirana ndi magulu osiyanasiyana pofuna kudziwitsa anthu za momwe matendawa akufalira komanso momwe angapewedwere.

Mneneri wa undunawu adatinso ukhondo ndiofunika kwambiri pankhondo yolimbana ndi matendawa komanso matenda ena onse omwe amafala chifukwa chosowa ukhondo.

Mkulu wa bungwe lomenyera ufulu wa zaumoyo wa anthu la Malawi Health Equity Network (MHEN) a George Jobe apempha kuti pakufunika kulimbikitsa ntchito yodziwitsa anthu zakuwopsa kwa nthenda ya masoyi chifukwa ilibe mankhwala eni eni.

"Nthendayi ndiyosavuta kupatsirana kwake ndipo imasokoneza umoyo wa munthu. Anthu sangathe kupita kuntchito, ophunzira sangathe kupita kusukulu ndipo ogwira ntchito zachipatala sangathe kupereka chithandizo chamankhwala pamene iwonso ali ndi matenda a maso, choncho pakufunika anthu adziwe zambiri za matendawa ndicholinga choti alimbikitse ukhondo mmakomo mwawo" adatero Jobe.

# Boma lipitiliza kulemba ndi kusamalira apolisi

YACHOKERA PA TSAMBA 1

muno.

A Chakwera anati mu ulamuliro wawo zaka zinayi zapitazi alemba apolisi okwana 6,000. Iwo anati apolisi ena okwana 2000, akhala akumaliza maphunziro awo mmiyezi itatu ikubwerayi.

"Dziko limene limakhala tchelu pankhani zachitetezo limayenera kukhala ndi achitetezo okwanira pofuna kukhazikitsa bata komanso kuwonetsetsa kuti malamulo akutsatidwa.

"Lamulo liyenera kukhala lamphamvu kwambiri kuposa ndalama, ndale, ngakhalenso kutchuka kuti tipange dziko lathu kukhala labwino kukhalamo. Ndikulowa pa udindo wanga, ndidalonjeza kulemba apolisi okwanira ndipo lero ndine okondwa kuti takwaniritsa izi," adatero a Chakwera.

Mtsogoleriyu adalangiza apolisiwa kuti akhale chitsanzo chabwino posunga mwambo komanso kulemekeza malamulo a ntchito yawo nthawi zonse kuti apereke chikhulupiliro kwa anthu omwe akuwatumikira mdziko muno.

A Chakwera anayamika ntchito yabwino yomwe apolisi akugwira powonetsetsa kuti anthu akusunga mwambo komanso kulemekeza malamulo. Iwo analonjeza kuti ulamuliro wawo upitiliza kupereka nyumba zabwino, kukweza mmaudindo komanso malipiro abwino kwa apolisi.

Mkulu wa Apolisi mdziko muno a Merlyne Yolamu anayamika mtsogoleriyu powonetsa chitsanzo chabwino popereka mwayi wantchito kunthambi zaboma zosiyanasiyana.



A Chakwera kupereka satifiketi kwa mmodzi wa apolisi

Iwo anati ali ndi chikhulupiliro kuti apolisi atsopanowa akathandiza kukhazikitsa mwambo ndi bata mdziko lino maka pomwe dziko lino likukonzekera zisankho chaka chamawa.

A Yolamu anapempha apolisiwa kugwira ntchito yawo modzipereka komanso mokonda dziko lawo.

Nduna yowona Chitetezo cha Mdziko a Ken Zikhale Ng'oma anayamikira mtsogoleriyu poyika chitetezo cha dziko patsogolo komanso kuwonetsetsa kuti apolisi akukhala mnyumba zabwino.

Pamwambowu, pomwe panalinso apolisi ena omwe anamaliza maphunziro awo kuchokera kusukulu za Mtakataka komanso Mlangeni, Mtsogoleri wadziko lino anapereka ma satifiketi kwa apolisi 35 omwe anachita bwino kwambiri pamaphunziro awo.



# Ulimi wa Chamba udzichitika motsata malamulo

YACHOKERA PA TSAMBA 1

pamene ukufunikirabe kwambiri kumisika yambiri yamayiko akunja chifukwa cha ubwino wake, "adatero a Dimba.

Iwo adatinso kukambirana kodzama pankhaniyi kudachitika zaka zinayi zapitazo ndipo akuyembekezera kuti mtsogoleri wa dziko lino avomereza lamuloli.

Mtsogoleri wa nyumbayi, a Richard Chimwendo Banda, adalongosola bwino kuti lamuloli silikuloleza kunyamula kapena kugwiritsa ntchito chamba mwamsangulutso koma likupereka chilolezo kwa anthu omwe ali ndi ziphaso okha kuchita nawo ulimiwu.

"Chomwe aMalawi akuyenera kumvetsetsa ndichakuti kulima chamba kupitirira kukhala kosaloledwa mdziko muno koma lamuloli likulola kuchita ulimiwu motsatira malamulo okhwima kuti Amalawi apewe kugwiritsa ntchito mbewuyi mosayenera," adatero a Banda.

Mneneri wa chipani cha United Democratic Front (UDF), a Nedson Poya, anadandaula za kukwera kwa ndalama zomwe munthu akuyenera kupereka kuti apatsidwe chiphaso cha ulimiwu.

Iwo adati lamulo lovomereza ulimiwu likufuna kuthandizira kugwiritsa ntchito mbewuyi popangira mankhwala osati kulimbikitsa kusuta pakati pa achinyamata ngati momwe ena akuganizira.



Wojambula: Nkhokwe yathu

Ulimiwu uzichitika motsatira malamulo - Chimwendo

Pazokambirana za a phungu ku nyumbayi, mafunso adabuka okhudzana ndi kagwiritsidwe ntchito kachamba, zomwe zidapangitsa kuti aphungu awunikire zambiri pa lamuloli.

Aphungu a boma adawunikira kuti pakhale malamulo othandiza alimi akumidzi komanso kuwalimbikitsa paulimiwu ndicholinga chakuti uwapindulire.

ZA BOMA

# Nkofunika kukumbukira omwe adataya miyoyo ndi Freddy - Chakwera

WOLEMBA:
ALEX CHITWERE

POZINDIKIRA mavuto ambiri omwe anthu adakumana nawo chifukwa cha Namondwe wa Freddy mdziko muno, Mtsogoleri wadziko lino Dr Lazarus Chakwera posachedwapa adatsogolera mtundu wa Amalawi pamwambo wachikumbutso patatha chaka chimodzi chichitikireni ngoziyi.

Mwambowu omwe udasonkhanitsa azipembedzo, andale ndi ena onse pamodzi unachitikira ku Mulanje. Ili ndi boma limodzi limene lidakhudzidwa kwambiri ndi namondweyu.

A Chakwera adati kunali kofunika kwambiri kuti mwambowu uchitike pofuna kulemekeza miyoyo ya anthu yomwe idatayika pangoziyi. Mtsogoleriyu adati ndi zomvetsa chisoni kuti ena mwa amene adataya miyoyo ndi anthu omwe ankagwira ntchito zopindulira ndi kuthandiza mabanja awo.

"Tidataya anthu amene amapindulira mabanja awo komanso dziko choncho nkofunika kuwalemekeza mwapadera," adatero a Chakwera.






Wojambula: Alex Chitwere

Dr Lazarus Chakwera ndi Mai wafuko Monica Chakwera anali nawo kumwambowu komwe atsogoleri amipingo anatenga mbali yaikulu

Mtsogoleri wa dziko linoyu, adatinso ndi okondwa ndi momwe mabungwe osiyanasiyana amdziko muno komanso ochokera mayiko akunja adaperekera thandizo pangoziyi.

Iwo adati: "Ndikuthokoza kwambiri chifukwa cha thandizo limene tikupitirirabe kulandira. Ndichenjeze Amalawi ena omwe akutibwezeretsa mmbuyo pofuna kusokoneza thandizo limeneli. Pamene ena asonyeza chidwi chofuna kutithandiza, tisamatseke chitseko ngati kuti zonse zili bwino."

Iwo adatinso boma ndilokonzeka ndikufunitsitsa kumaliza ntchito yokonza milatho, misewu, zipatala, sukulu ndi zina zonse zomwe zidawonongeka pa nthawi ya namondweyu.

Wapampando wa bungwe lowona zachakudya padziko lonse la World Food Programme (WFP), a Paul Turnball, , adayamikira mgwirizano omwe Amalawi adasonyeza pobwera pamodzi ndikusonkhanitsa chuma chawo kuti apereke thandizo kwa anthu omwe adakhudzidwa ndi ngoziyi.

"Bungwe lathu mogwirizana ndi Boma lakhala likuwonetsetsa kuti anthu akuthandizidwa munyengo yovutayi ndipo kuti akukhala moyo wabwino. Ndipo tipitilira kuonetsetsa kuti anthu akuthandizidwa moyenera," adatero a Turnball.

Mfumu yaikulu Kaduya, idati anthu a m'madera omwe adakhudzidwa akufunikabe thandizo popeza akuyambanso umoyo wina ndipo ng'amba yomwe yachitika chaka chino ikuperekanso chiwopsezo pa moyo wawo.

Namondwe wa Freddy adaononga kwambiri kumwera kwa dziko la Malawi mwezi wa Malichi chaka cha 2023, pomwe katundu ndi miyoyo idatayika.

# Nduna ipempha adindo alimbikitse ukhondo mzipatala

WOLEMBA
LEONARD MASAULI

KUSOWA ukhondo ndi chimodzi mwa zomwe zimathandizira kufalikira kwa matenda osiyasiyana. Mmbuyomu dziko lino lavutika ndi nthenda ya kolera ndipo pano kuli chiopsezo chifukwa chakufala kwa nthenda ya maso.

Mchaka cha 2022 kufikira 2023, dziko la Malawi linataya anthu opyola 1,700 chifukwa cha nthenda ya kolera yomwe inafala kwambiri chifukwa chakusowa ukhondo mmadera ambiri.

Kusowa ukhondo mmadera ambiri omwe anakhudzidwa kunadza chifukwa cha vuto la madzi abwino zomwe zimapangitsa kuti anthu azigwiritsa ntchito madzi osatetedzeka.

Boma ndi mabungwe amakhala nthawi zambiri akugwirira ntchito limodzi mavuto oterewa akagwa pofuna kutetedza miyoyo ya anthu.

Pachifukwachi, bungwe la Water Aid posachedwapa linakonza nkumano ofuna kugawana nzeru pankhani zolimbikitsa ukhondo mmalo osiyanasiyana komanso mzipatala mdziko muno.

Nduna yazaUmoyo a Khumbidze Kandodo Chiponda, pankumanowu analimbikitsa adindo kuchilimika potengapo mbali kuwonetsetsa kuti mzipatala muli ukhondo okwanira pofuna kupewa matenda omwe odwala angawatengere mzipatala monga kolera.

A Chiponda analimbikitsa adindo komanso mabungwe kuyikapo chidwi kwambiri powonetsetsa kuti akupereka madzi abwino mzipatala ngati njira imodzi yolimbikitsa ukhondo komanso kuchepetsa matenda.

ZA UMOYO



Wojambula: Leonard Masauli

Mai Khumbidze kandodo kuyendera ziwonetsero za zaumoyo

"Nkhani ya madzi abwino komanso ukhondo, komanso kupereka thandizo labwino pachipatala zimadalira madzi. Tiyamikire mabungwe omwe akugwira ntchito yabwino yopereka madzi abwino monga a Water Aid," adatero a Chiponda.

Ndunayi inati adindo mzipatala amalekerera posayika ndondomeko zokonzanso mijigo ndi mipope zikaonongeka zomwe anati zimasokoneza kagwiridwe ka ntchito koyenera.

Mkulu oyendetsa ntchito za Water Aid kuno ku Malawi, a Peter Phiri, anati nkumanowo unali ofunika kwambiri chifukwa unapereka mayankho amomwe adindo angathandizire kulimbikitsa ukhondo mzipatala komanso kupereka madzi abwino.

Iwo analimbikitsa mabungwe ndi ena onse kuti alimbikitse kugwirira ntchito limodzi pothandiza kukweza ukhondo mdziko muno.

"Vuto la madzi ndilalikulu mmadera ambiri mdziko makanso mzipatala zathu. Adindo akuyenera kuchilimika pantchito yothetsa mavuto amenewa," adatero a Phiri.

Iwo analimbikisa kuti ngakhale ndikofunika kulimbikisa ukhondo komanso ndikoyenera kuyika ndondomeko zabwino zokonza zipangizo monga mijigo komanso mipope yamadzi zikawonongeka.

ZA ULIMI

# Mitengo yambewu yatsopano yapereka chimwemwe

WOLEMBA
BRIGHTON CHIMSINDE

Chaka ndi chaka boma limakhazikitsa mitengo yogulira ndi kuguliritsira mbeu yomwe alimi komanso ochita malonda ogula ndikugulitsa mbeu amayenera kutsatira.

Mitengoyi imayikidwa ngati njira imodzi yowonetsetsa kuti alimi sakuberedwa komanso akupeza phindu kuchokera kuzokolora zawo.

Mchaka chino cha 2024, boma lidatulutsa chidziwitso cha mitengo yoyambira kugulira mbeu zomwe zikololedwa mchaka cha 2023/2024.

Wapampando wa khonsolo ya m'boma la Mchinji,a Dorothy Musa, wayamikira mitengo yogulira mbeu ya chaka cha 2023/2024 yomwe boma lakhazikitsa.

Musa wati mitengo yatsopanoyi ithandiza kuti mavenda asamagule zokolola za alimi pamitengo yosavomerezeka m'bomalo.

"Tikuthokoza boma chifukwa cha mitengo yomwe yayikidwa ngati yoyambira kugulira mbewu komanso kuti idatulutsidwa munthawi yake chifukwa mavenda ayamba kale kubera alimi. Ndizomvetsa chisoni kuti mavenda amagula zokolola za m'minda pamtengo wotsika pogwiritsa ntchito sikelo zabodza," adatero a Musa.

Iye anachenjeza mavenda kuti khonsolo yawo siyisekelera aliyense yemwe akuchita zosayenera powagula alimi mbewu zawo pamitengo yachinyengo.



Wojambula: Brighton Chimsinde

Mitengo yatsopano ya mbewu itukula alimi - Mussa

Iwo anati akuluakulu a khonsoloyi ali okonzeka kuteteza alimi kwa mavenda omwe amagwiritsa ntchito sikelo zosavomerezeka.

"Tiwonetsetsa kuti alimi, makamaka ang'onoang'ono apindule ndi mitengo ya chaka chino," adatero a Musa.

M'modzi mwa alimi a m'bomali, Alumackio Kalonga, wa mmudzi mwa Robert 4, Mfumu yayikulu Zulu anathokoza boma pokonzanso mitengo yogulitsira mbewu zawo.

"Chaka chatha chimanga chinali pa K500 pa kilogalamu imodzi ndipo chaka chino chafika pa K650, pamene mtedza wosaswa ndi nyemba zili pa K1,200 kuchoka pa K950 ndi K700 pa kilogalamu. Mutha kuwona kuti ndi matumba atatu a mtedza nditha kukwanitsa kugula matumba a feteleza," adatero a Kalonga.

Malingana ndi chidziwitso chomwe chachokera kuboma ndimlandu kugula zokolola kwa alimi pamtengo otsika kuposa mitengo yokhazikitsidwa.

BOMA LATHU Nyuzipepala

Mlangizi
William malimero

Mkonzi
Daniel Kasondo

Dizayinala wamkulu
Eugene Makwakwa

Dizayinala wachiwiri
Annie Kakolo


Nyuzipepalayi imafalitsidwa ndi Unduna wa Zofalitsa nkhani

*P/Bag 310, Capital City, LL3*
***www.ict.gov.mw***

*Boma Lathu nyuzipepala inakhazikitsidwa ndicholinga chophunzitsa ndi kudziwitsa mtundu wa Amalawi popititsa patsogolo ntchito za chitukuko.*


























# Zina mwa zomwe zachitika mdziko muno posachedwapa

**1** *Dr. Lazarus Chakwera ndi Mai wafuko la Malawi pamwambo okumbikira anthu amene anatisiya pangozi ya namondwe wa freddy*

**2** *Mtsogoleri wadziko lino kulandiridwa ndi wachiwiri wawo a Saulos Chilima ku Mulanje.*

**3** *A Chakwera anali nawo ku mwambo wanjira ya mtanda omwe unachitikira ku Lilongwe.*

**4** *Dr Lazarus Chakwera kotsegulira malonda a fodya ku msika wa Chinkhoma, ku Kasungu.*

**5** *Mtsogoleri wa dziko lino ndi wachiwiri wawo, a Saulos Chilima kukhazikitsa sukulu ya anthu ogwira ntchito m'boma ku Lilongwe*

**6** *Dr Lazarus Chakwera kuima limodzi ndi a kazembe a maiko a Burundi, Mexico, Gambia ndi Spain*

**7** *Anthu kuyenda ndawala yosonyeza umodzi patsiku lokumbukira wayilesi, ku Mzuzu*

**8** *Achinyamata amene angomaliza kumene maphunziro a ntchito ya polisi kuguba pa mwambo omaliza maphunziro awo*

**9** *Amayi a Chipani cha Malawi Congress kulandira mtsogoleri wadziko lino ku mwambo okhazikitsa damu ku Dowa*

**10** *Nyakwawa yayikulu Chilima (Dr. Benson Chilima) ndi mkazi wawo pamwambo ovekedwa ufumu.*

**11** *A Chilima kupereka mphatso kwa mtsogoleri wa bungwe la zachitundo la Rotary International a Gordon McInally*

# Ntchito yoteteza mtsinje wa Bua ili mkati

WOLEMBA
WANANGWA TEMBO

ZA CHILENGEDWE



Wojambula : https://nkhani.blogspot.com/2012/02/bua-river.html

Mtsinje umayenera kukhala otetedzedwa ndi zachilengedwe mmbali ngati mitengo ndi zomera zina

MUDZI wa Chivunika kwa Mfumu yaikulu Njombwa ku Kasungu uli pakati pamapiri a Chimphako ndi mtsinje wa Bua. Mudziwu ndi wa asodzi komanso alimi.

Mfumu yammudziwu, a Chivunika, omwenso ali mlimi, adati kwa zaka zambiri, mtsinje wa Bua wakhala ukuyenda mosalekeza ndipo umathandiza mudziwu pa ulimi wamthirira komanso usodzi.

Lero, a Chivunika ndi ankhawa chifukwa chakuonongeka kwa nkhalango mmapiriwa, kumene kwaika ulimi awo pachiopsezo popeza madzi omwe amachokera kumapiriwa akukokolola nthaka mminda yawo.

"N'zokhudza kuona kuti zinthu siziri monga momwe zimakhalira mmbuyomu. Tawononga mitengo yonse ya mmapiri zomwe zapangitsa kuti mapiriwa akhale ndi makhwawa omwe amatsikira kuminda yathu.

“Kumbali ina, madzi othamangawo amanyamula zinyalala zambiri zomwe zimathera mumtsinje wa Bua ndipo pang’onopang’ono mtsinjewu unayamba kukwiririka. Izi zakhudza ntchito yathu yopha nsomba ndi ulimi wamthirira,”adatero a Chivunika.

Nawo Mayi Jessie Banda a m’mudzi mwa Kamzoole adagwirizana ndi a Chivunika kuti mitengo yakhala ikuonongeka kwambiri m’mapiri makamaka chifukwa cha ulimi wa fodya, kukulitsa malo olimapo, kudalira nkhuni, kutchisa fodya komanso kuwotcha njerwa zomwe zikuchepetsa zokolola zawo chifukwa malo ambiri olima adaonongeka.

Mkulu wa za chilengedwe m’boma la Kasungu, a Herbert Bolokonya, adati mtsinje wa Bua ukuonetsa zizindikiro zakuwonongeka kwa chilengedwe ndipo uli pa chiopsezo, makamaka chifukwa cha kukokoloka kwa dothi chifukwa cha kulima m’mphepete mwa mtsinjewu ndi kudula mitengo mwachisawawa.



Mayi kukumba dzenje lokololera madzi munkhalango

A Bolokonya anati ndikofunika kuzindikira kuti kuteteza mtsinje wa Bua sichisankho chabe koma chinthu chofunikira koposa kwa adindo onse komanso anthu omwe amapindula nawo popeza, mtsinjewu uli ndi kuthekera kwakukulu kopangira mphamvu zamagetsi ndi kugwiranso ntchito paulimi wamthirira.

“Ngati tingapitirire ndi mchitidwe umenewu, mtsinjewu ukhoza kuyamba kuchepa madzi. Pakufunika kuchitapo kanthu mwachangu kuti mtsinjewu ukhale otetedzedwa ndi okhazikika ndi cholinga chakuti mibadwo yamtsogolo idzapindule nawo," adatero a Bolokonya.

Mothandizidwa ndi ntchito yosamala chilengedwe yomwe ogwira amalandira ndalama anthu a m’dera la Chivunika adatenga udindo oteteza minda yawo ndi mtsinje wa Bua.

Mlembi wa m’derali, a Mike Mdambo, adati cholinga chawo ndi chotetedza tsogolo lawo posunga zinthu zachilengedwe zomwe zimathandizira pa miyoyo yawo.

“Takonza makhwawa omwe adapangidwa mmapiri a Chimphako omwe amatsikira m’minda yathu ndi kubzalanso mitengo 21,000 m’mapiri komanso kufupi ndi mtsinje wa Bua. Tikukhulupirira kuti izi zithandiza kuchepetsa madzi osefukira ndi kutetedza minda yathu komanso kupewa kusefukira kwa mtsinje,” adatero a Mdambo.

Iwo adafotokozanso kuti anthu ammudziwu adakhazikitsa malamulo olanga anthu amene angaononge mitengo ndi kulimbikitsa alimi kuti azidyetsera ziweto zawo m’malo ovomerezeka kuti nkhalango zawo zibwererenso mwakale.

Ntchito yobwezeretsa chilengedweyi ili ndi mamembala 500, omwe 300 mwa iwo ndi Amayi. Dera la Chatalala ndi limodzi mwa madera 23 omwe akugwira nawo ntchitoyi. yomwe ndi gawo la ndondomeko yowona za chithandizo chaumoyo wa anthu imene idakhazikitsidwa ndi boma ndi thandizo la banki yayikulu padziko lonse ya World Bank.

Ntchito yobwezeretsa chilengedweyi ikufuna ithetseretu zoopsa za kusintha kwa nyengo zomwe zimawopseza miyoyo ya anthu pamene ikulimbikitsanso kuti anthu ovutikaw ndi mabanja omwe ali pachiwopsezo athe kukhala odziimira paokha.

Kudzera muntchitoyi madera a m’bomali akuyembekezeka kubzala mitengo yosachepera 500,000

Monga momwe anthu a m'madera la Chatalala akuwonetsera, kusamala zachilengedwe ndi udindo wa aliyense kotero kuti pakufunika mgwirizano, luso lamakono, ndi kudzipereka kwa aliyense powonetsetsa kuti chilengedwe chikusamalidwa ndi kutetezedwa kuti chidzapindulirenso mibadwo yamtsogolo.



# Anthu aku Dedza asangalala ndi mlatho watsopano

WOLEMBA
STEVE CHIROMBO

DEDZA ndi limodzi mwa mwa maboma omwe anthu akhala akukumana ndi mavuto amayendedwe chifukwa chakusowa kwa milatho mmadera ena. Anthu a mdera la Chipeni Mfumu yaikulu Kaphuka akhala ali pavuto lalikulu pofuna kuyenderana chifukwa chosowa mlatho pa mtsinje wa Nadulu.

Pofuna kuthana ndi vutoli khonsolo ya Dedza idayamba kukonza mlathowu omwe tsopano awumaliza. Mlathowu omwe ndi wandalama zokwana 36 miliyoni kwacha zomwe ndi ndalama zochokera mthumba la chitukuko cha bomali, udaperekedwa kwa anthu akuderali.

Kwa nthawi yaitali, anthu am'madera a Ntapo, Chipeni ndi Kamfundula akhala akuvutika pantchito zambiri zamiyoyo yawo zomwe zimafunika kuwoloka mtsinje wa Nadulu. Mwachitsanzo, ana a sukulu amajomba osapita kusukulu nthawi yamvula chifukwa chakusowa mlatho pamtsinjewu.

Wapampando wa Khonsolo ya Dedza, a Themuka Nkhwewu anati anali osangalala powona kuti ntchito ya mlathowu inafika kumapeto ndipo kuti tsopano anthu ayamba kugwiritsa ntchito mlathowo.

“Mlathowu uthandiza anthu kuyenderana ndi kulumikizana mosavuta mmaderawa posiyana ndi kale pamene amavutika kwambiri kuti awoloke mtsinjewu,” anatero a Nkhwewu.

Iwo anathokoza Boma popereka chitukuko cha mlatho kuderali, pomwe anati uthandiza kutukula ntchito zamalonda.

“Mavuto ndi ambiri mdziko muno ndipo zimatengera utsogoleri wabwino kuti zitukuko zotere zipite kumadera mosasankha. Mlatho wa Nadulu ndi gawo limodzi la ntchito zachitukuko zomwe khonsolo yathu inayika mu mndandanda wa zitukuko zaboma lino ndipo tikuwonetsetsa kuti ntchito zake zizikhala zapamwamba ndi zokhalitsa,” Nkhwewu anatero.

Nyakwawa yayikulu Chipeni, inati kwa nthawi yaitali akhala akuganiza kuti milatho yabwino imaganiziridwa kumangidwa mmatauni mokha koma kumangidwa kwa mlathowu kuderali ndi loto lomwe lasanduka chinthu chogwirika ndi kubweretsa chimwemwe kwa anthu mderali.

ZA CHITUKUKO



Wojambula: Steve Chirombo

Mlatho watsopano pamtsinje wa Nadulu, ku Dedza

“Mayendedwe sakhalanso ovuta kudera kuno. Kusowekera kwa mlathowu linali vuto lalikulu kwambiri pakati pathu ndipo ana athu pano azipita ku sukulu mosavuta,” Iwo adatero.

Mkulu owona mapulani ndi chitukuko m’boma la Dedza, McPherson Mwakhwawa anayamikira anthu akuderali chifukwa chotenga nawo mbali pachitukuko cha mlathowu, pomwe anati zimathandizira kuti ntchito ikhale yabwino ndi yapamwamba.

ZA ULIMI

# Boma lipereka K6.5 biliyoni ku magulu a Alimi



Alimi kuwonetsa macheke a ndalama zomwe alandira

WOLEMBA
ALIKO MUNDE

KWANTHAWI yaitali alimi kudzera mmagulu akhala akuvutika pofuna kupeza ndalama zopititsira patsogolo ntchito zawo kuti apeze phindu lochuluka pakamodzi.

Kafukufuku wakhala akuwonetsa kuti mdziko muno muli magulu a zamalonda koma ena sakuchita bwino chifukwa cha kuchepekedwa kwa ndalama zoyambira kapena kutukulira ntchito zawo za malonda.

Kwa nthawi yoyamba Boma ndi thandizo lochokera ku Banki yapadziko lonse ya World Bank, kudzera ku ntchito yotukula ulimi ya Agriculture Commercialization (AGCOM) lidakhazikitsa ntchito yotukula magulu abizinesi mdziko muno ngati njira imodzi yofuna kutukula maguluwa.

Nduna yaza Ulimi a Sam Kawale posachedwapa, anapereka ndalama zokwana K6.5 biliyoni kuti zithandize kutukula ntchito zamagulu makumi anayi ndi mphambu imodzi (41) ochokera mmaboma khumi ndi atatu (13) mdziko kuno.

Mwa zina, ndalamazi zithandiza maguluwa kupeza misika komanso kutukula ntchito za mabizinesi awo.

Poyankhulapo, mdera la Mfumu yaikulu Nankumba m’boma la Mangochi, a Kawale anati iwo ndiwokondwa kuti tsopano ntchito yopititsa patsogolo ulimi ngati bizinesi ikutheka molingana ndi masomphenya ndi ngodya za mndondomeko ya chitukuko ya 2063.

Iwo anati kudzera kuntchito ya AGCOM, alimi ambiri tsopano atukuka chifukwa azipeza phindu paulimi wawo.

“Masomphenya athu amu 2063 amatsindika kulimbikitsa ulimi wamakono pofuna kuti alimi azipeza zokolola zochuluka komanso kupeza misika yokhazikika, ndichifukwa chake tikupereka ndalama kwa alimi kuti ziwathandize kukwaniritsa maloto awo.

“Kudzera kuntchito ya AGCOM, tikufunanso kuti alimi asinthike pochita ulimi ngati bizinesi ndipo tayika ndalama zopyola K600 biliyoni zomwe tipereke ku magulu a bizinesi muzaka zingapo zikubwerazi,” adatero a Kawale.

Ndunayi inati ndiyokhutira kuti kudzera kuntchitoyi, Malawi adzakhala wodzidalira pa chakudya komanso alimi adzapeza phindu lochuluka.

Mkulu oyendetsa ntchito yotukula ulimi ya AGCOM, a Dr Ted Nakhumwa analimbikitsa anthu mderali kuti alembere ku ofesi yawo ngati akufuna thandizo la ndalamazi pokhazikitsa ndi kukhala mmagulu a anthu makumi awiri (20) pagulu lili lonse.

Iwo anati kudzera kuntchitoyi mchaka chatha cha 2023, alimi ambiri athandizika ndipo miyoyo yawo yasintha.

Paulendowu, a Kawale anayenderanso sikimu ya mthilira ya Mlambe yomwe ikuyendetsedwa ndi a Greenbelt Authority ndipo boma likufuna kutukula ntchito za ulimi wamthilira m'derali omwe ndi malo ochuluka mahekitala 800.

# Umphawi ukulimbikitsa nkhanza ku ana

WOLEMBA
ANDREW MKONDA

“Takhala moyo ozunzika kwambiri ongokhalira kuzungulira mmakomo mwa anthu kusaka maganyu kuti tipeze ndalama yogulira zovala, chakudya komanso makope. Moyo wathu wakhala wovuta kwambiri mpakana nthawi zina timagona ndi njala,”

Umu ndi mmene moyo wa Major Lyton wadzaka 11 komanso Yamikani Dyless wadzaka 13 ochokera mmudzi wa Mfumu yayikulu Chitekwere m’boma la Lilongwe udaliri chifukwa awiriwa adabadwa m'banja labambo yemwe samasamala za ana awo.

"Kuyambira nthawi imene mayi athu adatengana ndi bambo athu otipezawa, moyo wathu ndi ovutika kwambiri. Ine ndi azing’ono anga onse anayi tidasiya kupita kusukulu,

Zambiri timadzipangira tokha kudzera mmaganyu omwe timapanga tsiku ndi tsiku. Bambo athuwo nawo amadalira maganyu kuti pakhomo papezeke chakudya,” anadandaula motero Dyless misonzi ili mmaso.

Iye akuti posachedwapa anatsogozana ndi Major kuyenda mtunda okwana makilomita 80 kuchokera kwa mfumu yayikulu Chitekwere kupita kwa Mfumu yayikulu Chadza ndicholinga chokapeza maganyu.

“Tidachoka kwathu kupita mmudzi mwa a Chatha komwe tidapeza ganyu yoweta ng’ombe. Sizinali zophweka chifukwa timachoka mmawa kupita kukadyetsa ng’ombe kunkhalango komwe timakakhalako ndi njala tsiku lonse lathunthu,” adafotokoza Dyless.

Itamva za mavuto omwe anawa amakumana nawo, khonsolo ya boma la Lilongwe idagwirana manja ndi anthu ena akufuna kwabwino ndikuwasiyitsa anyamatawa ntchito yoweta ng’ombe yomwe inali nkhanza kwa anawo.


Wojambula: Vincent Khonje

Ana a sukulu kupereka mauthenga otsutsana ndi nkhanza


Wojambula: Vincent Khonje

Yamikani ndi Major ali ndi makolo awo pakhomo lawo

Mkulu oyang’anira zakagwiridwe kantchito m’boma la Lilongwe, a Chiletso Mbewe ati kuwalekelera ana komanso kulephera kuwapatsa thandizo lokwanira ndizina zomwe zikupititsa patsogolo nkhanza za ana mdziko muno.

“Ndizomvetsa chisoni kuwona kuti mabanja ambiri omwe alibe kuthekera kosamalira ana ndiomwenso akumakhala ndi ana ambiri. Izi zimapangitsa kuti anawo adziyendayenda kusaka ndalama zogulira zofuna zawo za tsiku ndi tsiku,” anatero a Mbewe.

Kafukufuku wa nkhanza za ana omwe anachitika mchaka cha 2022 anwonetsa kuti pakufunika kuchirimika mu nkhondo yothana ndi nkhanza za ana. Ana oposela 2.1 miliyoni a zaka zapakati pa 5 ndi 17 ndi omwe akukumana ndi mavutowa.

Kafukufukuyi anawonetsanso kuti kugwiritsa ntchito ana achichepere kumachulukira kwambiri kumabanja ovutikitsitsa.

ZA UMOYO

# Ntchito ya Tsogolo La Ana ipereka K87 miliyoni

WOLEMBA
PETRO MKANDAWIRE

MAPHUNZIRO ndi ofunikira kwambiri pa chitukuko chadziko liri lonse. Koma ntchito yamaphunziroyi imakumana ndi mavuto osiyanasiyana monga kuchepa kwa nyumba zophunziriramo ndi ena.

'Bwenzi amaoneka pamene uli pamavuto', akulu anatero. Ichi ndichifukwa, ngakhale udindo othetsa mavutowa ndi wa Boma, abwenzi ena amabwera kuno kwathu kuzathandiza pantchito yotukula maphunziro munjira zambiri.

Mmodzi mwa abwenziwa ndi dziko la Germany lomwe linakhazikitsa ntchito ya 'Tsogolo La Ana', pofuna kuthandiza boma kutukula maphunziro mmaboma a Blantyre, Chiradzulu, Phalombe, Lilongwe, Mulanje, Thyolo ndi Salima.


Wojambula: Petro Mkandawire

Pa sukulu ya Mariya ku Blantyre pakhala zipinda zatsopano

Tsogolo la Ana posachedwapa yakhazikitsa ntchito yowonjezera nyumba zophunziriramo pa sukulu ya Mariya mdera la Mfumu yaikulu Kuntaja ku Blantyre yomwe ndi yandalama zokwana K87 miliyoni.

Sukulu ya pulayimale ya Mariya idamangidwa ndi Tsogolo La Ana mchaka cha 2022 ndipo ili ndi makalasi anayi okha, kuyambira sitandade 1 mpaka 4. Kumangidwa kwamidadada yowonjezera muntchito yatsopanoyi, kupangitsa kuti sukuluyi ikhale ndi makalasi onse mpaka sitandade 8.

Mkulu oyang’anira ntchitoyi, Lucy Maunde anati anaganiza zowonjezera makalasiwa ataona kuchuluka kwa ana pasukuluyi.

Iwo anati ophunzirawa akafika mu sitandade 5 amasowa kolowera kuti akapitilize maphunziro awo zomwe zimalimbikitsa anawa kusiyira maphunziro panjira.

“Tiperekanso ma desiki okwana zana, mabuku ophunzirira komanso a aphunzitsi ndi mipando ya aphunzitsi kungotchulako zochepa chabe,” Maunde adatero

Mlangizi wa sukulu za pulayimale mdera la Dziwe, m’bomali, Snowden Chimaimba, anati zipinda zowonjezerazi zithandiza ana omwe anasiya sukulu kubwereranso.

“Ntchitoyi ichepetsa mtunda omwe ana amayenda kupita ku sukulu zina komanso itukula dera lino pamaphunziro,” anatero Chimayimba.



# Bungwe lakumudzi lakangalika kubwezeretsa chilengedwe

WOLEMBA
GIFT MKULICHI NDI
MEMORY KHUTULIWA

BUNGWE la kumudzi la Nankumba kwa Mfumu yaikulu Somba ku Blantyre liri pa ntchito yobzala ndi kusamalira nkhalango yomwe anabzalako mitengo yosiyanasiyana.

Bungweli lomwe ndilammudzi mwa Namonde likuchita izi pomemedza ndi kulimbikitsa anthu kuteteza nkhalango ku mchitidwe odula mitengo mwachisawawa, kuwotcha makala ndi kuyatsa moto mnkhalangamo.

Wa pampando wabungwe la Nankumba Community Based Organisation (CBO), John Machika anayamikira mafumu a mderali ndi magulu oyang’anira za chilengedwe ammudzi (Village Natural Resources Management Committtes) pa chimvano chomwe chilipo pa ntchito yotetedza nkhalango ya mmudziyo.

“Ndithokoze Mfumu yaikulu Somba potipatsa malo amene tinakhadzikitsapo nkhalangoyi. Komanso tithokoze alangidzi a zamitengo pa ntchito yopereka ulangidzi wa zankhalango kuyambira pa nthawi yomwe tidakhadzikisa nazale ya mitengo mu 2017 kufikila lero pamene tikusimba lokoma chifukwa cha nkhalango yathuyi,” anatero Machika.

Wapampandoyu anawonjedzeranso kuti nkhalangoyi yomwe ili ndi mitengo yosiyanasiyana izathandiza anthu a mmudzimo pa ntchito zosiyanasiyana monga kupeza milimo komanso izathandiza sukulu zamkomba phala ammudzi kupeza nkhuni zophikira phala.

Anthu ozungulira nkhalangoyi yomwe lili pansi pa Nankumba CBO akuti akhala akudzala mitengo mmapiri, mphepete mwa mitsinje ndi mmakwawa komanso msukulu ndi mmakomo ngati njira inanso yopititsa patsogolo ntchito yodzala mitengo ndi kusamalira zachilengedwe.

Nkhalango ya kwa Nankumba ili mdi mitengo pafupifupi 10,000 yomwe inabzalidwa mchaka cha 2017 ndipo ina mwa mitengo yomwe ili mu nkhalangoyi ndi kesha, ntangatanga, blue gum, tsamba, m’banga ndi nsangu.

Mmodzi mwa alangidzi a Nankumba CBO, bambo John Chipeta adapempha Boma komanso mabungwe omwe si aboma kuti atengepo mbali pothandidza magulu akumudzi monga la Nankumba panchito yosamalira za chilengedwe popereka upangili, zida zogwirira ntchito komanso ndalama zothandizira pa ntchito yobzala mitengo komanso pa ntchito zina zosamalira za chilengedwe

Iwo anati bungwe la Nankumba limagwiritsa ntchito zida zawo zomwenso ndi zosakwanira pa ntchito yolambulira m’mphepete mwa nkhalango komanso kupalira mitengo yaing'ono.

“Ndipemphe Boma komanso mabungwe kuti athandidze Nankumba CBO ndi mawilibala, zikwanje, mafosholo, jombo, zovala pogwira ntchito kuti anthu adzikwaniritsa kugwira ntchito yobzala mitengo komanso kutetedza nkhalango mopanda vuto,” adatero a Chipeta.

Mlangizi wa za nkhalango wa dera la Milare, Samuel Maliro adanena kuti ndi chinthu chabwino pamene anthu a kudera akukangalika ndi zinthu zotukula dera lawo monga ntchito yosamalira nkhalango momwe Nankumba CBO ikuchitira.

Iye anawonjedzeranso kuti nkhalango za mmudzi ndizofunika popeza zimabweretsa chuma ngati zitamasamaliridwa bwino, popeza anthu atha kumakolola nkhuni komanso kuikamo ming’oma ya njuchi.

A Maliro adathokoza Nankumba CBO pogwiritsa ntchito upangiri omwe iwo amapereka ndipo adati izi zinapangitsa kuti Nkhalango yi ikhale yochititsa chidwi.

Mafumu ndi anthu odzungulira nkhalango ya Nankumba anakhazikitsa malamulo otetedza nkhalango kuti yemwe angapezeke akudula mitengo azayenera kutengeredwa ku bwalo la Mfumu kukaimbidwa mlandu ndikupereka chindapusa cha mbuzi

Nankumba CBO inapempha Boma ndi mabungwe komanso anthu akufuna kwabwino kuti apereke njinga zamoto kwa ena mwa mamembala ake omwe amakhala madera akutali kuti adzikwanitsa kuyenda mosavuta pa ntchito zotumikira anthu a kuderako pankhani yosamala nkhalango ndi zachilengedwe zina.

Iwo akupemphanso zipangizo zogwirira ntchito yoweta njuchi pofuna kupititsa patsogolo phindu la nkhalango yawo komanso ngati njira yopedzera chuma choyendetsera gulu.

Gulu la Nankumba lidakhadzikitsidwa mchaka cha 2000, ndipo pano liri ndi mamembala okwana 40 ndipo mwa mamembala amenewa 12 ndi abambo pomwe 28 ndi amayi.

ZA CHITUKUKO


Wojambula: Gift Mkulichi ndi Memory Khutuliwa

Mamembala bungwe la Nankumba kuyendera nkhalango yawo





Mitengo yachilengewe yomwe bungwe la Nankumba likusamala




Mamembala a bungwe lakumudzi la Nankumba

# Kanema yachimalawi yatsopano ituluka posachedwa

WOLEMBA
SHEMINAH NKHOMA NDI
LEVISON LESTER

KUONERA kanema kwasanduka chimodzi wa zinthu zomwe anthu ambiri a mtauni ndi kumudzi komwe akuchikonda. Izi ndi monga masewero omwe amabweretsa msangulutso pakati pa anthu.

Zambiri mwa zomwe anthu amaonera zimakhala zoti zajambulidwa kunja kwa dziko lino ndipo izi zikuwapangitsa a katswiri ojambula kanema a kwathu kuno kuti asatsalire mmbuyo koma kuyetsetsa kujambula ndikutulutsa kanema ogwirizana ndi zochitika za kuno ku Malawi.

cholinga chachikulu ndi chakuti aMalawi aziowonera kanema ogwirizana ndi ndikupititsa patsogolo chikhalidwe chathu.

Ojambula kanema a mdziko muno akonzeka kutulutsa kanema ina yomwe mutu wake ndi ' Chilungamo' ndi cholinga chofuna kudziwitsa anthu zakuipa kwa mchitidwe wozembetsa anthu mdziko muno.

Poyankhula ndi wokonza kanemayi, Brazio Mathias Kanyong'o anati kanema yawo ndi pachimake penipeni pa msangulutso komanso ili ndi mbali zambiri zophunzitsa mtundu wa Amalawi..

"Tinaganiza zojambula kanemayi kuti tidziwitse anthu za mchitidwe wozembetsa anthu pakuti ambiri ambiri samamvetsa bwino za nkhaniyi ndipo ena sadziwaso kuti izi zikuchitika mdziko muno," Kanyong'o adatero.

Iye adati anthu aluso la zolembalemba ndi lokonza kanema ali ndi udindo woyika poyera zoipa zomwe zimachitika pakati pa anthu mdziko muno.

"Kanemayi ndiyofunikira kwambiri kumtundu wa aMalawi. Anthu azaluso ali ndikuthekera kopereka uthenga kwa anthu mosavuta. Taganiza zotulutsa kanemayi ndi cholinga chophunzitsa anthu," Kanyong'o adatero.

Mtsogoleri wa bungwe lowona za Kanema mdziko lino, Gift Sukali yemwe amadziwika kuti Sukezi anati akatswiri ojambula kanema akuyetsetsa kugwira ntchito yabwino potulutsa makanema apamwamba zomwe zikupangitsa kuti ntchito yawo iziyamikiridwa.

"Tikuona makanema achimalawi ochuluka akutuluka ndi nkhani zokhudza chikhalidwe chathu. Zimenezi zikuwonetsa kuti ntchito yathu ikupita patsogolo mdziko muno," iye adatero

Kanemayi akuyembekedzeka kudzawonetsedwa koyamba mmwezi wa Juni chaka chino.




Kanyong'o



Mtsogoleri wa bungwe lowona za Kanema mdziko lino - Gift Sukali

MPONDO

Peter Nyakhuwa








## Ophunzira pasukulu yaukachenjede akondwa ndikukwera kwa ndalama

WOLEMBA
ELIA CHIBWE NDI
SELLAH CHUNDA

Ophunzira msukulu za ukachenjede akhala akudandaula chifukwa chakukwera mtengo kwa zipangizo zogwiritsa ntchito pamaphunziro awo komanso moyo wawo watsiku ndi tsiku.

Powona mavuto omwe ophunzirawa amakumana nawo, boma kudzera mu Unduna waza Chuma posachedwapa lidalengeza zakuwonjezera kwa ndalama yangongole yothandizira pa maphunziro awo kuchoka pa K350,000 kufika pa K560,000, zomwe zasangalatsa makolo komanso ana ophunzirawa.

Kuwonjezeraku kupereka chilimbikitso kuti tsopano achinyamatawa akwanitsa kuthana ndi ena mwa mavuto omwe amakumana nawo pamaphunziro.

Ena mwa ophunzira pa sukulu ya ukachenjede ya University of Malawi (UNIMA) ati iwo ndiwokondwa ndikukwera kwa ndalamayi chifukwa tsopano azikwanitsa kulipirira malo ogona, kugula chakudya ndi zipangizo zina zofunika pamaphunziro awo.

Malinga ndi kalata yomwe analemba atsogoleri amabungwe oyimirira ophunzira anzawo, ophunzirawa ayamikira Boma poyika chidwi chake pa umoyo wa ophunzira am'sukulu za ukachenjede zaboma m'dziko muno.

Kuyankhula m'malo mwa ophunzira anzake pa sukulu ya Malawi University of Business and Applied Sciences ( MUBAS), Gershom Nyirenda anati kukwera kwa ndalamayi kuthandiza kupititsa patsogolo maphunziro ndi umoyo wa ophunzira omwe ali ovutika m'sukulu za ukachenjede.

Iye anati: "Kukwera kwa ndalamayi kukhala kwaphindu kwambiri kwa ophunzira ambiri mdziko muno chifukwa tsopano akwanitsa kugula zofunika zawo za tsiku ndi tsiku zomwe zithandize kupititsa maphunziro awo patsogolo. Ophunzira amakumana ndimavuto ochuluka akakhala alibe thandizo lokwanila koma apa zili bwino kwambiri kuti Boma latiganizira." anatero Nyirenda



Wojambula: unima.ac.mw

Imodzi mwa sukulu za ukachenjede ya University of Malawi

Mtsogoleri wabungwe la ophunzira pasukuluyi, Elia Mwalwanda naye anayamikira mtsogoleri wadziko lino, Dr. Lazarus Chakwera pakumva ndikuyankha pempho lawo.

Mwalwanda adati iye ndiokondwa kwambiri ndiyankho lomwe iwo alandira kuchokera kwa mtsogoleriyu lomwe lapangitsa kuwonjezera kwa ndalamayi.

"Ndife okondwa chifukwa tsopano chiwerengero cha ophunzira omwe adakatha kusiyira sukulu panjira chifukwa chakusowa thandizo tsopano chichepa. Ambiri mwaophunzira amakhala kunja kwa sukulu komwe amalipira malo ogona mokwera kwambiri. Kuwonjezera kwa ndalama yangongoleyi adzikwanitsa kudzisamala paokha,"Mwalwanda anatero.

Mneneri wabungwe lopereka ngongole kwa ophunzira msukulu zaukachenjede, a Millie Kasunda anatsindika zakufunika kwa ngongole yomwe bungwe lawo limapereka kwa ophunzirawa ponena kuti zimathandiza ophunzira kupeza zina mwa zofunika pamaphunziro.

A Kasunda adalimbikitsa ophunzira onse omwe ali osowa kuti aziyetsetsa kupempha ngongoleyi ngakhale atakhala kuti iwo ndi ophunzira akale kapena ongoyamba kumene maphunziro awo.

Iwo adati chaka chino cha 2024 kufika 2025, bungwe lawo lakonzeka kupereka ngongolezi kwa ophunzira osachepera 30,000.

ZA MASEWERO

## Aphunzitsi a mpira wamiyendo alandira maphunziro a CAF

WOLEMBA
BENI BAMUSI

OFESI yowona zamasewero m'boma la Thyolo posachedwapa inapereka maphunziro a CAF-D kwa aphuzitsi 58 ochokera m'madera osiyanasiyana m'bomalo ndi cholinga chotukula masewera a mpira wamiyendo.

Polankhula pamaphunzirowa ku sukulu ya sekondale ya Adolorata, DC wa boma la Thyolo, a Hudson Kuphanga, anati anali okondwa ndi maphunzirowo chifukwa atukula masewero a mpira wamiyendo m'bomalo .

Iwo anati chosangalatsa ndi chakuti aphuzitsiwo tsopano aziphunzitsa bwino luso lamasewerowa ku matimu akumadera kwawo.

"Ndikofunika kuyambitsa mpikisano wachikho pamasewerowa m'bomali ndicholinga choti matimu azionetsa luso lomwe azilandira kuchokera kwa aphunzitsiwa," anatero a Kuphanga.

Iwo anati ayetsetsa kupempha mabungwe osiyanasiyana omwe ali m'bomalo kuti awathandize kukhadzikitsa chikho choti matimu m'bomali azilimbirana pamasewerowa.

"Pamene tikutukula magawo ena, sitiyenera kuiwala zamasewero. Eni minda ya tiyi komanso mabanki omwe ali m'boma lino atithandiza paganizo lathu lotukula masewerowa," iwo anatero.

A Kuphanga anati pamene bwalo lamasewero labomali latsala pang'ono kutha, bomali likuyenera kukhala ndi ligi yomwe idzabweretse ndalama ku khonsolo yabomali.

Mkulu wa zamasewera m'boma la Thyolo, mayi Olga Mlambe, adati ofesi yawo idakonza maphunzirowa itazindikira kuchepa kwa aphuzitsi a masewero a mpira wa miyendo m'bomalo zomwe zikulepheretsa chitukuko chamasewerawa m'bomali.



Wojambula: Beni Bamusi

Ena mwa a phunzitsi a mpira wa miyendo omwe analandira maphunziro a CAF-D

A Mlambe anapempha thandizo la zipangizo zosiyanasiyana monga mipira, ma yunifulomu ndi zipangizo zina za masewerowa zomwe zingathandizire aphunzitsi a mpira wa miyendo kuwonetsa luso lomwe aphunzira.

"Tawapatsa luso, koma pali zambiri zoti zichitike. Choncho ofesi yanga ikupempha anthu akufuna kwabwino kuti atipatse zipangizo zina zomwe zitithandize kukwaniritsa luso lomwe aphuzitsiwa apeza," adatero.

Mmodzi mwa anthu omwe anali nawo pamaphunzirowa a Fatsani Chisale ochokera ku sukulu ya sekondale ya Mapanga, anayamikira maphunzirowa ponena kuti awapatsa luso latsopano lowathandiza pa ntchito yawo ya uphunzitsi wa mpira wa miyendo.

Mwa aphunzitsi a mpira wa miyendo 58 wa, 44 ndi aphunzitsi a m'sukulu za pulaimale ndi sekondale pomwe ena onse ndi aphunzitsi a makalabu a m'bomali.

NYUZIPEPALAYI NDI YA ULERE CHONDE MUKAWERENGA PATSANI ANZANU AWERENGEKO

# MASEWERO



Aphunzitsi a mpira wa miyendo alandira maphunziro a CAF

« TSAMBA 15

VOL. 47 NO. 1 | *YAULERE* | Boma Lathu, Epulo, 2024

# FAM ipereka mipira kwa Aphungu



*A Haiya (kumanzere) kupereka mipira kwa Aphungu a Nyumba ya Malamulo*

WOLEMBA
TWIMEPOKI MANGANI

MASEWERO osiyanasiyana akamachitika anthu amabwera pamodzi posatengera kusiyana kwa mitundu, zikhulupiriro ngakhalenso zipani zomwe amatsatira. Powona chikoka chomwe chili mmasewero ammadera akumidzi ngakhalenso mtawuni, bungwe lowona za masewero ampira wa miyendo mdziko muno la Football Association of Malawi (FAM) laganiza zotukula masewerowa kumadera komwe aphungu aku Nyumba ya Malamulo amaimirira.

Masiku apitawa, bungweli lidapereka mipira kwa Aphungu a Nyumba ya Malamulo ngati njira imodzi yotukulira masewerowa mmadera mwawo.

Mtsogoleri wa bungwe la FAM, a Fleetwood Haiya, adachita izi pamkumano omwe udachitikakira ku nyumbayi posachedwapa pamaso pa Nduna ya za Masewero a Uchizi Mkandawire, Sipikala wa Nyumba ya Malamulo mayi Catherine Gotani Hara ndi Nduna zina.

FAM idapereka mipira isanu kudera lirilonse la Aphungu onse 193 pofuna kutukula masewera a mpira wa miyendo.

A Haiya adatsindika zakufunika kopereka zipangizo za mpira wa miyendo kusukulu ndi matimu ampira mmaboma kuti athe kupititsa patsogolo luso komanso kulimbikitsa anthu kutenga nawo mbali pamasewerawa.

"Tikukhulupirira kuti kuyika chuma chathu pamasewera a mpira mmadera akumidzi ndikofunika kwambiri kuti masewero a mpira mdziko muno apite patsogolo. Mipira yomwe taperekayi ipereka mwayi kwa achinyamata kutukula luso lawo ndikupititsa patsogolo pamasewerowa," anatero a Haiya.

Nduna yaza Achinyamata ndi Masewero, a Uchizi Mkandawire adayamikira zomwe bungwe la FAM likuchita potukula masewero ampira wamiyendo mdziko muno makamaka kumadera a kumudzi.

"Boma lithandizana ndi bugwe la FAM pa zitukuko zonse zomwe likuchita pofuna kupititsa patsogolo masewera a mpira. Nkhani ngati zimenezi sizimangolimbikitsa kuchita masewera olimbitsa thupi komanso zimalimbikitsa achinyamata athu kuchita zinthu pamodzi," adatero a Mkandawire.

Kuwonjezela pa zipangizo zomwezi, bungwe la FAM lidati liri ndi chidwi chofuna kugwirizana ndi Aphungu a Nyumba ya Malamulo kuti akhazikitse mfundo zolimbikitsa chitukuko cha mpira mmadera awo.

Sipikala wa Nyumba ya Malamulo Mayi Gotani Hara adagwirizana ndi ganizo la bungwe la FAM potsindika zakufunika koyika malamulo othandizira kuyendetsa bwino mipikisano ya mpira kumadera ammidzi pofuna kuthana ndi mavuto omwe amadza chifukwa chopanga zinthu mwachisawawa.

"Ndikofunikadi kuti FAM igwirizane ndi aphungu poyendetsera limodzi masewero omwe amachitika mmadera awo kuti mipikisano yampira wa miyendo izikhala ya dongosolo," adatero a Gotani Hara.